TRUTH CENTERED TRANSFORMATION

BUKU 1



CHIYAMBI CHA UTUMIKI WOFIKILA MUNTHU YENSE WAPHUMPHU

BUKU LA OPHUNZIRA

Zamkatimu

Phunziro 1 ..... Nkhani Yonse……3

1.1 Chitsogozo cha kukambilana kwa magulu ang'ono 5

1.2 Sewero: Adamu ndi Hava 3

Phunzito 2: Anthu ndi ofunika kwa Mulungu..... 6

2.1 Chitsogozo cha zokambilana..... 6

Phunzilo 3: Kukonda Mulungu ndi kukonda abwenzi athu 7

3.1 Seweto la Mlaliki..... 7

3.2 Chitsogozo cha zokambilana..... 8

Phunzilo 4: Luka 2:52 9

4.1 Chitsogozo cha zokambilana..... 9

4.2 Mndandanda wa kakulidwe 10

Phunzilo 5: Mulungu akufuna mpingo uthandizepo: 11

5.1 Kuphunzira kuzera mu nkhani 11

5.2 Bokosi la Njira zothandizira.....13

Phunziro 6: Kodi ndi thandizo lina liti limene tingathandize? 15

6.1 Mbusa Wong.....15

6.2 Kuphunzira kudzera mu nkhani:Jose&Maria 18

Phunziro 8: Kunvetsetsa mmene tingathandizile 19

8.1Mai Lee:chitsogozo cha Zokambilana. 19

8.2 Banja limene lili ndi chosowa: Kutsogolera kukambilana.....20

Phunziro 9:Ntchito zachikondi.....21

9.1 Maonekedwe a ntchito za chikondi.....21

Phunziro 10: Chikonzekero ndi ndondomeko ya ntchito za chikondi 24

10.1 Ma fomu ochitila ndondomeko.....26

Phunziro 1: Nkhani Yonse

1.1 Kutsogolera

Chiyambi

Kutengera pazimene taphunzira kuchokera pa Genesis 1-2 , kodi inuyo mungayankhe bwanji mafunsowa?.

- Kodi dziko linali ngati chiyani pachiyambi cha dziko mmunda wa Eden?
- Kodi ubale unali motani pakati pa Mulungu ndi Adam?
- Kodi ubale pakati pa Adam ndi Hava unali otani?
- Kodi ubale pakati pa Adam ndi Chilengedwe unali otani?

Kugwa/Kuchimwa kwa Munthu

Kuchokera mu nkhaniyi komanso ndi zina zimene timawerenga kuchokera m'baibulo , kodi ndi mabvuto ati amene anthu amakumana nawo chifukwa cha kugwa kapena kuchimwa kwa Munthu?.

- Werengani Genesis 3:8,10 –kodi ndi chiyani chomwe chinachitika pa ubale wa munthu ndi mulungu pa nthawi imene munthu anagwa

- Werengani Genesis 3: kodi ndi chiyani chomwe chinachitika pa ubale wa munthu ndi munthu mzake pa nthawi imene munthu anagwa

- Werengani Genesis 3:15 – Kodi chinachitika ndi chiyani pa ubale wa pakati pa munthu ndi chilengedwe pa nthawi imene munthu anagwa/kuchimwa.?

Utumiki

ABRAHAMU –Werengani Genesis 12:1-3- Mu ndime imeneyi , mulungu akumuzutsa Abrahamu ndikumudalitsa . Ndi chifukwa chiyani iye akumudalitsa Abrahamu?.

MOSE

- Kodi Lamulo limangokhudza zauzimu okha basi kapena limakhudzanso ubale wathu pakati pa munthu ndi munthu mzake komanso chilengedwe?.

- Werengani Deutreronomo 28:1-14 . Kodi mulungu akuti zotsatira zidzakhala chiyani pamene titsatira malamulo amenewa? Kodi malonjezano amene Mulungu anapeleka ndiokhudza zinthu za uzimu zokha kapenanso zinthu za kuthupi?.

Werengani 2 Mbiri 7:14

- Kodi ndi ndani amene Mulungu akuwauza kuti azichepetse ndikupemphera?.

- Kodi Mulungu ananena kuti ndi chiyani chimene chidzachitike ngati iwo akhala omvera?

Mtanda

Werengani Akolose 1:19-20. Kodi ndi chifukwa chiyani yesu anafa.

Kubwerelanso

Werengani Chibvumbulutso 21:1-7

- Kodi pamapepo , ubale wa Mulungu ndi munthu udzakhala otani?

- Kodi ubale wa munthu ndi munthu nzake udzakhal otani?.

- Kodi ubale pakati pa munthu ndi chilengedwe chidzakhala chotani? Kodi tidzakhala ndi chokudya chokwanira? Kodi tizizadwalanso?

Phunziro 1: Nkhani Yonse:

1.2 Sewero: Adam ndi Hava

“Kukambilana pakati pa Adamu ndi Hava”	
Adamu:	(Kulima) Hava,Ananva kuwawa pogwira ntchito mmunda atatha kudya chipatso chomwe mulungu anawaletsa!
Hava:	Eya ,ndi anyamata athu sadzapedzanso mtendere nthawi zones . Iwo anakangana ndi kumenyana wina ndi mzake nthawi zonse. Ine ndikukhulupirira kuti kukangana kwao sikunafike koipa! Ndipo iwo anavala masamba ankuyu-Iwo anali ndi maonekedwe osasangalatsa.
Adamu:	(Kutsutsana) chabwino, sitingakwanitsenso kugula zovala zatsopano , ndiye musadandaule! (Takhalani chete)ine ndisowa masiku aja akale , pamene Mulungu amayenda nafe ndikumalankhula nafenso. Tsopanotu nayenso ali ndi chisoni kuti ndife anthu omangoyendayenda. Ndipo takumbukira mmene zinyama zimatinverera? Tsopano lino zimatithawa chifukwa chodwabwa nafe!
Hava:	Eya, ngakhale kutiluma kumene!Uuuhi…Ndimadana ndi njoka! Sindimakhulupirira kuti ndinanvera malangizo a njoka!zonsezitu ndichifukwa cha kulakwitsa kwa njoka!
Adamu:	Ayi, ndi olakwitsa ndi iweyo! Sunachite chinthu cholondola! Ndinganvere bwanji malangizo a munthu amene ananvera malangizo anjoka?.
Hava:	Chabwino , koma musandiloze chala ine . amene munalakwitsa ndinu!(kuima , mwachisoni) pepani- sizikuthandiza kungokalipa. Adamu , kodi ukuganiza ngati zinthu zizakhalanso mmene zinthu zinalili poyamba?.
Adamu:	Sindikudziwa- ndi mulungu yekha amene angakonze chinthu chimenechi!
Hava:	Oohihi! Ayi-ndichani tsopano?(kukuwa ,kuthamangira panja)tasiyani kumenyana inu anyamata! Siyani pompano. Kodi mukundinva?ndikauza atate wanu , ndipo sakondwera ndi chimenechi!
Adamu:	(Kubwerela ku munda,kuyasamula) kugwira ntchito , ntchito , ntchito , ntchito ,ntchito…

Phunziro 2: Anthu ndi ofunika kwa Mulungu

2.1 Chitsogozo cha zokambilana Genesisi 1:26-27

- Kodi anthu asiyana bwanji ndi chilengedwe china? Kodi ndi chiyani chimene mulungu anagwilitsa ntchito monga chitsanzo polenga munthu?

- Kodi ndi zikhalidwe zina ziti zimene zimapezeka mwa Munthu zimenenso zimakhala mwa Mulungu?. Tapezani zochuluka mmene mungathere.

Werengani Masalimo 139:13-16

- Kodi vesi imeneyi ikutiuzanji za kufunikira kwa munthu?.

- Kodi mukuganiza ngati vesi imeneyi imakhudza anthu ena chabe kapena munthu wina aliyense?.

Kukambilana m'magulu ang'ono:

- Kodi ndi anthu ena ati amene samawerengeredwa?
- Kodi ndi njira ziti zimene tingaonetsere kwa anthu kuti ndiofunikira kwa Mulungu?.

Phunziro 3: Kondani Mulungu komanso konda mzako

3.1 Sewero la Mulaliki



Chiyambi cha ofotokoza nkhaniyi: a khristu nthawi zina amakhala ndi "kuona kochepetsa zinthu cha uthenga wabwino"amanvetsetsa kuti kulandila yesu ndi chiganizo cha moyo-kapena imfa , koma sanvetsetsa chinthu china chake. Ngati sanvetsera zosowa za amzao ndiye kuti uthenga wawo wataika…. Lero , tiyendera khomo la osauka. Khomo lokhalo , munthu osauka komanso akudwala ndipo ali pa kama. Mlendo , amene ndi Mlaliki wa Chikhristu amene akulalikila khomo ndi khomo, wangofika **mlaliki:** Odi! Odi! Kodi muli anthu muno ? ndingathe kulowa?(akulowa)

Munthu Osauka Odwala: (mofooka)lowani muno…

Mlaliki: Wawa. Ndine _____ kuchokera _____ Mpingo. Ndangobwera lero kuzaitanira wina aliyense ku mpingo kwathu. Mulungu wangotidalitsa ndi chitsitsimutso cha mphanvu .. Inu simungafune mutasemphana ndi chitsitsimutsochi.

Munthu Osauka Odwala : (Akubuula, akulankhula mwa ululu) Sindingathe kubwera , sindingathe kuzuka pa kama … ndadwalika kuti sindingayende …. Ndinachotsedwa ntchito … ndilibe ndalama zoti ndigule mankhwala..kapena chakudya….kapena kulipila nyumba yogona…

Mlaliki: awa ndi mabvuto akulu ndithu , koma ndikudziwa za wina wake amene ali ndi mayankho ku mabvuto a moyo uno. Kodi munalandila yesu monga mpulumutsi ndi mbuye wa moyo wanu?

Munthu Osauka Odwala: (Mofooka)banja langa , abale ndi abwenzi anandithawa mmene ndinadwala ndi kuchotsedwa nchito…..kodi pali wina wake wa mu mpingo mwanu amene angandithandize?chonde?.

Mlaliki:Thandizo labwino kwambiri limene mungapeze lili mu kabuki ka mau a mulungu aka. Kamafotokoza dongosolo lonse la mulungu pa moyo wanu. Mukudziwa, sichifuniro chake kuti inu mugone pa kama choterechi, Tengani , werengani , pempherani pemphero la ochimwa , ndipo khulupililani.

Munthu Osauka Odwala: (Mofooka)sindingathe….ndafooka kwambiri…(wasiya kulankhula , ndikungogona osasunthasuntha.)

Mlaliki: (anayang'ana misempha)adakali ndi moyo ! ambuye alemekezeke!, ndinabwera pano mu nthawi yoyenera kuti ndichitile umboni! Ndingosiya kabukuka ! kuli bwino ndizipita cholinga ndikafikile miyoyo ina yotaika.(nalankhula mokweza nkhutu mwa munthu odwalikayo) tikupempherelani. Kumbukirani kuti yesu ndiye yankho(kenako akumapita).

Munthu Osauka Odwala: (Kungomuyang'ana akutuluka , kubuula)ooooooohi! (sanachitenso kalikonse-kapena kamene chimene chimaoneka kufunikila

Phunziro 3:Kondani Mulungu,Kondani anzanu.

3.2 Chitsogozo cha kukambilana

Werengani ma vesi otsatirawa:

Mateyu 22:36-40	Marko 12:28-31,33	Luka 10:27
Mateyu 7:12	Aroma 13:9	Agalatiya 5:14

Kodi kusisyana ndi kufanana mu ndime zisanu ndi imodzi zimenezi?.

Kodi Yesu akuti lamulo ndi liti mwa awiriwa limene lili lalikulu kuposa linzake?.

Pamene lamulo ndi aneneri ukuphatikizidwa mu lamulo limodzi lalikulu , kodi lamulo limeneli ndi liti?

Kodi mukuganiza ngati ndi chifukwa chiyani yesu anaganiza zophatikiza malamulo onsewa mu lamulo limodzi?.

Phunziro 4: Luka 2:52

4.1 Chitsogozo cha kukambirana

1. Kodi kukula kwa Yesu kunachitika pompopompo kapena kunali kuchitika kwa kanthawi?

2. Kodi Yesu anakula munyengo yotani pa nkhani ya zofunika zakuthupi ndi kakhalidwe kake?kodi anali ndi magetsi kunyumba kwake? Kodi anali ndi chakudya chokwanila, kodi amatha kuwerenga ndi kulemba? Kodi anali ndi makolo ake omukonda.(kodi anapita ku sukulu ya ukachenjede?)

3. Kodi Yesu anali ndi zinthu zofunika kuti akwanilitse cholinga cha Mulungu pa iye? Ngati anali nazo , chifukwa chiyani? , ngati analibe chifukwa chiyani?.

4. Kodi ndi chuma chochuluka bwanji kuti mukafikile cholinga cha Mulungu?.

5. Yesu anakula mmagawo anayi , kodi tingathandize ena kukula mmadera amenewa? Kodi tingathandize bwanji?.

6. Kodi ngati makulidwe a Yesus anali ofunika ka nthawi , kodi ndi nthawi yochuluka bwanji imene Ikufunika kuti anthu ena akulenso?.kodi ndi nthawi yochuluka bwanji imene tingaikepo kuti tikuzile miyoyo ya anthu ena?.

Phunziro 4:Luka 2:52

4.2 Bokosi losonyeza makulidwe

Mndandanda	Magawo a kukula kwa yesu			
Za Kukula	Mzeru	Thupi	Mzimu	Khalidwe
Wekha				
Banja				
Mpingo				
Dera/ Mudzi				

Phunziro 5: Mulungu akufuna Mpingo uthandize

5.1 Kuphunzira kudzera mu nkhani

Nkhani Yoyamba: Chovala cha munthu osauka

Ma membala a mu mpingo umenewu amaziyetsa okha gulu laling'ono komanso loponderezedwa lachipembezo.Anali ndi mantha okatumikila kunja kwa chikhristu.Atatha kuphunzira kuti akuyenera kuonetsera chikondi cha Mulungu ku dera lonse , mbusa anafunsa azimayi kuti afufudze zomwe derail likufuna sabata yotsatirayo.

Mu mapemphero a sabata ya yotsatirayo, azimayiwa anapeleka lipoti kuti anapeza azimayi khumi ndi awiri a chimwenye (Hindu) amene wina aliyense anali ndi chovala chimodzi chachimwenye.Mu nyengo yotentha , zovala zimenezi zimayenera kuchapidwa tsiku ndi tsiku. Ngati mzimayi ali ndi chovala chimenechi chimodzi , ndiye kuti , amayenera kukhala mnyumba mpakana chovala chake chochapidwacho chitauma pa dzuwa. Mbusayo anapempha ngati pali azimayi mu kachisimo amene anali ndi zovala zitatu amene anakakwanitsa kuthandiza chimodzi kwa azimayiwa.Azimayi okwanila anazipeleka kuthandizapo pa chosowa chimenechi. Sabata yotsatirayo azimayi a mu mpingowu anayendera mnyumba za azimayi amene anali ndi chovala chimodziwa ndipo anawapatsanso chovala china.Azimayi achimwenye anakopeka mtima ndi chinthu chimene azimayi a chikhristuwa anaonetsa ndipo anawaitana azimayiwa kuti awapempherele. Azimayi ena achimwenye amene anali oyembekezera anapemphanso azimayi a chi khristuwa kuti apempherere anawo amene sanabadwewa.

Werengani Nkhani 2 – Madzi akudera

Mdera lina kunali bvuto lalikulu losowa madzi. Pakutha kuphunzira zofuna zamulungu mu mpingo kukafikira anthu , utsogoleri wa mpingo unaganiza kufufuza paokha kuti akakwanilitse kusowa kwa madzi. Anapeza penapake kuti kubwereka zizpangizo zokumbira zitsime ndi manja. Poyambilira anthu anakana ganizoli ndipo anaganiza kuti madzi anali okuya kwambiri. Ndipo anati ngati zitsime zokumba ndi manja ndi zotheka, ndipo anaganiza bwanji kusakumba ndi kale lomwe?ndipo utsogloeri wa mpingo unaganiza zoyetsera . anabwereka imodzi kwa imodzi chogwetsa chisilinda cha chitsulo ndi winji.anachipititsa kwa anthu ndipo anayamba kukumba kuti apeze madzi kutseri kwa tchalichi. Madzi anapezeka pafupi , mafiti makumi anayi ndi mphambu zisanu, ndipo aliyense anasangalala kwambiri , amene sakapemphera pa mpigopo sanasangalale , iwo anaganiza zakuti mwina akhristu a mu mpingowo sadzalola ena kugwilitsa ntchito madziwo.Koma mmalo mwake mpingo unaitana anthu akumudzi kuti agawane mwa mulungu



mdalitso wakutheka kwa chitsime. Posakhalitsa oimilia mmadera oyandikila anthu akumudzi anapempha atsogoleri a mpingo kuti awathandize kukumba zitsime mmadera mwina mwa anthu.Mpingo unavomereza. Chaka chisanathe , zitsime khumi ndi zitsanu zinakumbidwa ndi manja , china cholowa kwambiri kuposa ma fiti makumi asanu ndi atatu. Chifukwa choti mpingo unaonetsera chikondi cha mulungu kwa anthu , motero anthu anakhutitsidwa moti pamene mpingo waitana anthu a mderali kuzanva mau a mulungu , mpingowu umadzadza ndi anthu.anali ndi njala yodziwa za mulungu ndi anthu amene anapeleka madzi

- Kodi mipingo imeneyi inachitanji?
- Kodi inali mipingo yolemera?
- Kodi anagwilitsa ntchito zipangizo zanji?
- Kodi anachitilanji zinthu zimenezi?
- Kodi ndi chiyani chimene chinatsatila pa zimene iwo anachitazi?

Phunziro 5: Mulungu akufuna mpingo uthandize.

5.2 Bokosi losonyeza njira zothandizira.

Zofunika	Njira yomwe mpingo ungathandizilepo
Njala	
Ludzu	
wamaliseche	
Kusowa nyumba yogona	
Kudwala	

 Mndende	

Phunziro 6:Kodi ndi zina zosowa ziti zimene tingathe kuthandiza:

6.1 M'busa Wong

Mu mzinda wa ukulu wa Baririo munali m'busa wina ovutika amatumikila ka mpingo kakang'ono. Dzina lake anali wong. Wong mosakhalitsa anapita ndikukakhala kumudzi chifukwa choti amazinva kuti Mulungu wamtuma iye kukakhala kumeneko. Mpingo unali wa ung'ono wa anthu makumi anayi , iwo anali azimayi ndi ana , Wong anali ndi ntchito ziwiri , iye amagwila ntchito yoti mkazi ndi ana ake awiri athandizike , ndiponso iye amayetsetsa mwa mtima wake wonse kudyetsa nkhosa zake zazing'onozi. Tsiku lina. Monga mwa chizolowezi chake , iye anakhala ndi ola imodzi kulankhulana ndi Mulungu wake dzuwa lisanalowe , iye anadzuka , navala ndi kuyenda mwakachetechete modutsa nsalu yotchinga imene inawalekanitsa malo ogona iye ndi malo amene mkazi wake ndi ana amagona. Iye anayatsa nyali yachitini imene inali yodzadza ndi mafuta ndi kuikidwa tsanza , iye anayamba kuwerenga mau ochokera mbuku lopatulika . mmawa okhao wa tsiku ili , iye anali kuwerenga mau ochokera pa Yesaya 58 , ndipo anali kunva kulila kwa Mulungu pa mtundu w aka pembezedwe koyenera kumene iye akukufuna kuti kachitike. Uku ndi kusala kumene ine ndinakusankha ; kuti amasule maunyolo achosalungama ndi kumasula magoli onse , kumasula opondelezedwa ndi kuphwanya magoli onse. Kodi si chinthu chabwino kugawana nawo chakudya chathu kwa iwo ali ndi njala ndi osowa malo ogona kuwapatsa malo ogona-pamene mukuona wina ali wamaliseche , tinveke iye , ndipo izi sizichokera mu thupi ndi mwazi?. Wong anapitilila patsogolo , kuti mtima wake unalimba ndi maganizo ake , nanga zinachitika bwanji kuti mulungu anatha kusamalila anthu osauka pamene wong mwayekha anapezeka pakati pa aumphawi ndi ovutika chimene chinapangisa mtima wake kuti usweke?.Iye amkaziwa mmene anthu akumudzi amavutikila kuti akhale ndi moyo. Iwo analidi anthu oponderezedwa. Ngakhale iye sanali ndi chakudya chokwanila choti adyetse banja lake , ndipo kawiri kawiri amalephera angakhale kuwagulila iwo mankhwala amene iwo amkawafuna. Iye amanena "Kodi Mulungu ali kuti"? Kodi mau a Mulungu angabwere pakati pano kuti tiagwilitse ntchito za La Pavas !" mmene iye ali kulimba ndi maganizo akewo , panali kogogoda kwa pansi pansi pa chitseko. "Kodi ameneyu angakhale ndani amene akugogoda mmamawa?" , Wong ananena , iye anapita kukhomo, "Kodi ndi ndani"?, mau a mbali ina ananena kuti " ndine Yesu , Wong !" Ndani , anafunsa Wong. " Ndine Yesu, Wong!." Iye ananva mau . " Kodi ndiwe ndani kweni kweni?" anafunsa Wong. Mau anabwerezanso "Wong , ndine Yesu." Ndabwera chifukwa ine ndinanva kulila kwa mtima wako. Ine ndafuna undiuze ine za vuto limene limakuvuta iwe." Mau amene ndinawanvawo anali eni eni. Wong mosamalitsitsa anatsimikiza ndikutsegula khomo. Kukanali mdimabe ndipo Wong anatha kuona chithunzithunzi chokha koma icho chimaoneka ngati yesu amene iye anali akumuganizila " Lowani ambuye " Wong ananena iyayi Wong, ndifuna unditenge ndikundionetsa anthu akumudzi wanu, ndikundionetsa ine chimene chimakupangitsa kuti mtima wako usweke." Anakhala odabwabe , Wong , anagwilizana nazo namchenjeza. Tiyenera kuyenda mosamalitsitsa ife—kwakhalaa kukugwa mvula ya mphanvu , kunali kuterela kwambili ndiponso kunalibe zimbuzi zambili. Pamene iwo anayenda miseu ya Bariro , Wong anamuuza Yesus nkhani za nyumba zimene anazidutsa. Mu nyumba iyo , mukhala mzimayi amene akusamala ana ake. Mu nyumba yakugwayo muli bamboo woledzela amene amamenya mkazi wake

ndi ana ake akaleddzela kawiri kawiri. Uko kuli nyumba ya President amene amapezela anthu ndalama koma ndi munthu wa ziphuphu amene amalonjeza anthu akumudzi kuti awabweretsera magetsi koma ali ndi cholinga choabela ndikutenga ndalamazo ndikukaledzela nazo. Iwo anadutsa pa malo pamene m=panalibe nyumba pakati pa mudzi . Iko kayenera kukhala kadera ndithu koma kunali kodzadza ndi zinyalala zimene zimapeleka fungo loipa ndipo kumakhalanso makoswe. "Ukuiona nyumba ija , anafunsa Wong uku akuloza chinsakasa chimene chinali pamwamba pa phiri."

Mzimayi ndi ana anai amakhala kumeneko , denga lake limaukha kwambili. Iwo ndi osauka kwambili ,iwo ali ndi zochepa kwambili zoti adye kapena kuvala ndiponso nthawi zonse pafupipafupi iwo amadwala" Mu nthawi ino awiri ali pafupi ndi chisakasa chimene Ras Pavas anachimanga.mphepete mwa phiri.
Ali patali Wong analoza ndi chala chake. " Mmusi mwakemu ndikumene azimayi ndi ana amapita kukatunga madzi. Kunalibe kwina koti akhoza kukatunga madzi ku Las Pavas."

Wong anatembenukila ku mbali ina, koma iye ananva kunena kwa pansi pansi. Iye ananvetsera mauwo. Anali yesu –Yesu amalila. Wong ankatha kuona zinthu zomwe zimene zinapangisa mtima wake usweke , zomwezo zinapangitsa mtima wa yesu kusweka.

Wong anayamba kulankhula , koma yesu anankhumbatila Wong , anamuyang;ana iye ndi kuyankhula. "Wong,ndifuna iwe chokhumba cha mtima wanga , ine pa Las Pavas" Mwachangu anapezeka kuyang'ana pansi pa Las Pavas. Yesu anayamba kulankhula , ndipo Wong ankatha kuona zinthu zomwe Wong ankafotokoza- izo zinayamba kuchitika! Yesu analankhula za anthu a mu mpingo wa Wong monga osauka chisaukile- amagawana zinthu zimene iwo anali nazo ndi osauka anzawowo. Tsiku lilolonse iwo amasunga mpunga pang'ono ndikuika mchitini, pakutha pa mulungu umodzi , wina aliyense wa iwo amadzadza chitin chimodzi cha mpunga umene iwo amabweretsa ndikupeleka ku mpingo mu dzina la yesu kuti agawile anthu akumudzi amene anali ndi zochepa monga iwo anachita. Iwo anachitanso chimodzimodzi ndi sopo. Azimayi amu mpingo ankayendera azimayi amasiye kumudzi ndi kusankha iwo – kuwachapila zovala zawo , kuwaphikila ndi kuwasamalila ana awo pamene iwo anali kudwala. Yesu anakamba za kulembana ntchito ndipo wong ankatha kuona kuti anthu akugwila ntchito osati nchito yolipidwa malipilo okwera koma ntchito imene inabweretsa ulemelelo pa umunthu wawo ndikuapatsa malipil okwanila kuti zikumane ndizofunikila pa miyoyo yawo. Yesu ananena za nyumba ndipo Wong anaona zisakasa zimene anthu amagona panvula. Zimapangitsa kuti anthu avutike ndikuzizila.ndiponso anthu amagona pa mvula. Osati nyumba zongoyerekeza koma nyumba zotetezeka bwino ndi zosamalika. Yesu ankakamba za madzi ndipo mwachangu mu ndondomeko yake panali madzi amipope kumene azimayi ndi ana amatungako madzi otetezedwa bwino ndi oyera. Yesu anakamba za ukhondo, ndipo Wong ankatha kuona kuti kunali zimbuzi-Osati imodzi panyumba iliyonse koma zimbuzi zokwanila kuti wina aliyense atha kugwilitsa ntchito
Dzala la zinyalala limene linali pakati pa mudzi linatha , mmalo mwake panali mitengo yochepa ndipo ana anali kuseka ndi kusewera, kumen yapo mpira . Yesu anakambaso za miyoyo yosinthika , ndipo Wong anaona kuti azimayi amene anali kuchita uhule anayamba kupeleka thandizo kwa ana ake mwa njira yoyenera tsopano. Woledzera anasandulika abambo abwino okondeka. Presidenti wa ziphuphu uja anasiya kugwilitsa ntchito mwa chinyengo , koma anakhala munthu othandiza dera lake, ndipo yesu anati " Wong , yang'ana mpingo !" Wong anayang'ana mpingo unali wodzadza. Amuna anali mmenemo ! anthu anali achimwemwe. Iwo anali kulemekeza mulungu pa zabwino

zomwe anawachitila Pamene Wong amalalikila , kuphunzitsa ndi kuwatsogolera anthu ake mu uzimu , ndi kumvera kwa machitichito achikondi. Yesu anafotokoza, Wong , Masomphenya awo sanangobwera mwa mphumphu pokhapokha ine ndibwera , koma ichi ndi cholinga changa pa Las Pavas. Ndikufuna iwe kuti ugawe masomphenyawa ndikuyamba kutsogolera anthu aku Las Pavas kuti ayende mmenemo.
Wong anayamba kutsutsana nazo , " Koma ambuye ife ndife anthu osauka kweni kweni!" "Wong"Yesu anafunsa mwakachetechete , " Kodi ndi ndani amene anatsogolera ana a Israel kuoloka Nyanja yofila". Kodi ndi ndani amene anachulukitsa mikate ndi msomba ndikudyetsa amuna zikwi zitsanu osaphatikiza akazi ndi ana. Kodi ndi ndani anachulukitsa mafuta ndi ufa oti mkazi wa masiye wa ku zerefati akhale nazo zokwanila ndipo adyetse banja lake kwa zaka zitatu za njala?. Kodi ndani analetsa mphepo pa nyanja ya Galileya?." " Inu munachita ambuye," Wong anayankha , "kenako", Wong , ukhale onvera pa zimene ndakuuza iwe kuti uchite. Ugawane ndi ena zimene uli nazo,ngakhale zili zochepa . Lalikila uthenga wabwino kwa anthu ako mu zauzimu ndi zamthupi . ndipo ndidzachilitsa dziko lako!"

Wong ananva kulila kwa tambala . Mkazi wake anakhosomola ndikugwededza mbali ina ya msalu imene inakhala ngati ntchinga . Koma nyali yake itazima , kunabwera kuwala . Wong anayang'ana kcuti aone Yesu , koma sanathe kumuona iye . Iye anadabwa , kodi anali mmaloto ? kodi anali masomphenya? Iye sanadziwe , koma wong sanadziwe kuti iye anakumana ndi yesu ndipo iye anali ndikumvesetsa kwina pa zokhudzika kwa Mulungu ndi anthu osauka---- ndi masomphenya a thupi a mmene iye anali kutengera anthu ake pa chiwonesero chachikondi cha Mulungu Mu Las Pavas.

- Kodi ndi mabvuto ena ati amene analipo mu dera la M'busa Wong?tagawani mabvuto amenewa mmagawo anayi , uzimu,lakakhalidwe,zathupi ndi kaganizidwe.

- Kodi cholinga cha Mulungu pa derali chinali chiyiani? Taonani vuto lina lili lonse ndipo muone mmene yesu anaonetsera mayankho ake kuti angakhale.

- Kodid yesu anauza Abusa Wong kuti achite chiyani?

Phunziro 6: kodi ndi zinthu zina ziti zimene tingathandize

6.2 Kuphunzira kudzera mu nkhani: Jose ndi Maria

Nyumba ya Jose ndi Maria yangophysa posachedwa ; ndipo palibiletu chimene chinatsala , dzulo , iwowa, iwo ndi ana awo asanu- anakahala ndi abale awo. Komabe pali kale anthu khumi amene akukhala mu nyumba yaing'onoyi, ndiye palibe malo a anthu ena asanu ndi awiri. Jose ndimulimi ndipo anabzala kale mmunda mwake , koma padakali miyezi ina itatu imene yatsala kuti iwo akolole. Aononga ndalama zonse zomwe anali nazo kugula mbeu za kumunda kwake , ndipo zonse zimene iye analinazo zaphysa ndi moto.



Kodi ndi zinthu zina ziti zimene banja ili likusowa?

Kodi ndi zinthu zina ziti zimene zilipo mdera zomwe zingathandize?. anthu

- katundu

- zipangizo

Phunzilo 8:Kunvetsetsa mmene tingathandizile:

8.1 Chitsogozo cha zokambilana cha Mai Lee.

Taganiza nkhani za Mai Lee ndikukambilana mafunso awa:

1. Kodi Mai Lee anachitanji kwa banja lililonse mwa mabanjawa?

2. Kodi ndi chiyani chimene chinatsatira pa zomwe Mai Lee anachita?.

3. Kodi chikanachitika ndi chiyani ngati Mai Lee anangopeleka ndalama kapena chakudya kwa mabanjawo?

4. Kodi chikhala Mai Lee anawapatsa ndalama za sabata iliyonse kwa zaka ziwiri , kodi mukuganiza ngati anthuwa miyoyo yawo inakasintha monga mmene inachitilamu?.

5. Kodi zikusiyana bwanji kuthandiza ndi ndalama kapena mmene Mai lee anathandizila?.

6. Tangoyerekezani ngati ambili mwa ife tinakati tizichita ngati mai Lee – kuyendera mabanja , kumvetsera , kuyang'ana ndi kuyetsetsa kunvetsetsa mabvuto awo, ndipo kumayang'ana mayankho. Kodi dera lanu linakasintha motani?.

Phunziro 8: Kunvetsera kuti tingathandize bwanji.

8.2 Chitsogozo cha zokambila za Banja lili ndi chosowa

Pali banja limene limakhala pafupi ndi Tchalichi chanu . mamuna kawiri kawiri amakhala atachoka ndipo pamwezi kapena kawiri pa mwezi amabwera kwa masiku ochepa ndipo amabweretsa ndalama pang'ono pa banja lake. Banjali limasamalila ana awo atatu ndipo palibe wina aliyense mwa iwo amene amapita ku sukulu. Kawirikawiri anawo amayenda opanda nsapato ndipo atavalanso zovala zakutha. Nyumba yawo yathanso ndipo kawiri kawiri imaukha kwambiri kukagwa mvula . mukadutsa panyumbayi, mumanva ana akulila chifukwa anali ndi njala.

Kodi ndi zosowa ziti zimene banja limeneli lili nazo?.

Kodi ndi njira yanji imene mukanathandizira pokhala ngati mai lee ku banja limeneli?.



Phunziro 9:Ntchito za chikondi

9.1 Maonekedwe a ntchito za chikondi

1. **Zomwe zachitika kuonetsa chikondi chamulungu**
    - Kodi anthu a mdera lanu amene samapemphera amaganiza bwanji za akhristu a mderali? Nanga ndi chifukwa chiyani?

    - Kodi anthu amabwera ku mpingo opanda ? ngati amabwera , chifukwa chiyani? , nanga ngati samabwera , chifukwa chiyani?
    - Kodi anthu osapemphera amaganiza chiyani za mulungu? Kodi iwo amaganiza kuti maonekedwe a mulungu enieni ndi ati?
    - Kodi mukuganiza ngati anthu amdera lanu anakanena kuti chiyani ngati mpingo wanu utayamba kuchita zinthu zina zimene zalembedwa mu nkhani za ntchito za chikondi?.

    - Kodi ndi chifukwa chiyani tingakonde kutsogoza kuchita ntchito za chifundo kwa anthu osapemphera kusisyana ndi kwa anthu opemphera anzathu.

2. **Kuchita monvera Mulungu**
    - Kodi ndi chi fukwa chiyani Yesu akuti ndichofunika kuti ife tichite chimene mulungu watilamula?.

    - Kodi Mpingo unasankha bwanji anthu oti aonetseredwe chikondi cha Mulungu?.
    - Kodi kusintha kumene kunalipo ndikotani mderali?.

3. **Zachitika kudzera mu mphanvu ya mulungu**
    Yang'anani Yohane 15:1-8

    Kodi ndime imeneyi ikutiuzanji za zimene tingathe kuchita mwa ife tokha? Kodi mukuganiza ngati izi zitanthauzanji?.

    - Kodi tingabale bwanji zipatso zochuluka?.

- Mu Yohane 15:5 , Baibulo limati ; “ ngati munthu akhalabe mwa ine ndi ine mwa iye, abala zipatso zochuluka.” Kodi mukuganiza ngati zitanthauzanji kukhalabe mwa Mulungu?.

- Kodi tingadalile bwanji Mulungu mu ntchito zimenezi?.

4. **Chitani choncho kuti Mulungu atamandidwe.**
   Werengani Yohane 15:8
   - Kodi cholinga cha kubala zipatso zochuluka ndi chiyani?.

   Werengani Mateyu 5:13-16

   - Kodid timachitilanji zinthu zabwino?

   - Kodi cholinga chathu chikuyenera kumakhala chiyani pamene tichita ntchito zachikondi?.

5. **Zazing’ono ndi zophweka**
   - Kodi ndi chifukwa chiyani chomwe mukuyenera kuyamba mochepa ndimophweka ntchito zanu za chikondi?.

6. **Zachitika pogwilitsa ntchito zida zopezekelatu.**
   - Kodi ndichifukwa chiyani mukuganiza ngati chizindikilo china ndi chokuti zachitika ndi zida zopezekeratu?.zida zimene Mulungu anapeleka kale zosachokera kwa anthu ena ayi? Kodi mukuganiza ngati izi zingakhale zofunika motani?.

Kauniuni wa Zochitika

Taganizilani mfundo zimene zinapelekedwa mu nthawi imene timatsegulila phunzilo ili. Konzaninso magulu anu anthu awiri awiri. Ndipo sankhani zitatu mwa zochitika zimenezi kuti muziunikile. Lingalilani mafunso amenewa:

1. Kodi ntchito imeneyi ingathandize bwanji kuonetse chikondi cha Mulungu ku dera? Kodi ndi chiyani chimene chingasinthidwe kapena kuonjezeredwa ku ntchito imeneyi kuti chionetsere chikondi cha Mulungu?.

2. Ndi chisanzo chiti cha ntchito yaing'ono komanso yophweka?.

3. Kodi ndi zinthu ziti zimene zikufunikila kuti ntchito zimene zikuchitika mdera lanu zimalizike?.

4. Kodi chochitika chimenechi chikusintha bwanji dera lanu?.kodi uku ndiye kusintha kumene inu munakafuna kuona mdera lanu? Ngati sichoncho , kodi chochitika chimenechi chingasinthidwe motani kuti chifikile ndi kusintha dera lanu?.

5. Kodi tingaziwe bwanji ngati tikuchita chochitikachi mu chifunilo cha Mulungu?.

6. Kodi mukuganiza ngati Mulungu angalemekezeke pomalizitsa chochitika chimenechi?.

Phunziro 10: Kukonza ndondomeko ya ntchito ya chikondi

10.1 Ma fomu andondomeko

1. Werengani ma sitepe a ndondomekowa
2. Kambilanani mfundo za ntchito za chikondi kuti mukonze ndondomeko.
3. Pempherani
4. Onani ngati mfundo zanu zikugwilizana ndi maonekedwe aja a nchito za chikondi
5. Yambanipo kupanga ndondomeko za ntchito yanu ya chikondi.
6. Pempherani.
7. Gawanani ndi ena za ma dongosolo anu ndikufunsa ena kuti anene maganizo awo.
8. Pempherani

Dongosolo la ma sitepe

Sitepe 1:Pemphero

Chinthu choyamba kuchita ndi kupemphera.tsopano yambanipo kupemphera.Mupempheni mulungu akuonetseni chomwe mukuyenera kuchita pa ntchito yanu ya chikondi

Sitepe 2: Sankhani chochita

Monga gulu, ganizirani chomwe mungapange monga ntchito ya chikondi.tayang'anani ziganizo zina izi zomwe munalemba mu phunziroli "Mulungu akufuna mpingo uthandize"ndipo kodi zofunika zina ndi ziti mu derali,"Limodzi , gwilizanani pa chimene mukunva ngati mulungu akukutsogolerani kuti

Mukasankha mutu , onetsetsani kuti chikhale chinthu chomwe mungachite mu masiku awiri kapena limodzi. Ngati sizingatheke masiku awiri ndiye kuti mungosankhapo ma sitepe ochepa okha amene mungakwanitse.

Sitepe 3: Ganizani chomwe chikufunika

Kuti tiyambe kukonza ndondomeko. Choyamba , tikuyenera kuganiza kuti tichitenji ku ntchitoyo-ndi anthu otani amene akufunika,ndi zinthu ziti zomwe zikufunika, chilolezo cha ndani chomwe chifunika, ndi zina zotere..kuti zikuthandizeni kuganizila chithu ichi , mukhoza kugwiritsa ntchito pepala ya mabokosi yomwe ili mbuku la ophunzila, mukatha kulemba mmalowa ndi zonse zimene mukufuna , ndiyeno mutha kuganizila kuti ndi ndani amene akayng'anile komanso ndi tsiku liti limene ntchitoyi izathe.

Sitepe 4: Lembani ndondomekoyo.

Onetsetsani kuti ndondomeko yanu iyankhe mafunso awa.(ngati gulu lili ndi kuzindikila kochepa , ndiye kuti sizofunikila kwambili kuti ndondomekoyi ilembedwe , koma mungoonetsetsa kuti anthu onse akambilana mafunso onsewa.

- Kodi muchita chiyani?
- Kodi mufunika chiyani kuti muchite chinthuchi? Mukatenga kuti zinthu zimenezo?
- Kodi mukukathandiza ndani?, nanga mwawafunsa kale?.
- Ndindani amene atenge nawo mbali pothandiza?.
- Kodi ndi liti limene inu mukachite ntchitoyi?.

Sitepe 5: Pempherani

Mukangotha kulemba ndondomeko,khalaninso ndi nthawi yopemphera, mufunseni mulungu kuti akuthandizeni kumalizitsa ntchitoyi ndikuchulukitsa zotsatira. Pempherani kuti zina lake likalemekezedwe. Mu sabata yotsatilayo kapena masabata awiri mmene mukukonzekera ntchito yanuyi,mupemphere kuti mulungu akuthandizeni mu ntchitoyi.

Sitepe 6: Chitani Ntchitoyo

Sitepe yotsatira ndiko kuchita ntchito imene munakonza ija. Yambani tsiku lanu ndi pemphero ndikupeleka mphanvu zanu zonse kwa Mulungu.Kumbukilani kuti mukuchita ntchitoyi kuti muonetsere chikondi cha Mulungu ku dera lanu. Yetsetsani kuchita khalidwe limene likukwanilitsa cholinga chimenechi.

Sitepe 7: Kuchita kauniuni ndikulemba mmene zinthu zayendera.

Siteoe yotsiriza ndiko kuunikila ndikulemba za mmene ntchito yayendera.Ndichifukwa chiyani timachita kauniuniu?. chifukwa izi zimatithandiza kuphunzilapo. Tikhoza kuganizila zimene tinachita bwino ndipo zomwe tingathe kuchita kuti tizachite bwino moposa nthawi ina.Sizitenga nthawi yaitali , ndi mphindi zochepa chabe mukhoza kungokambilana mafunso awa:

- Ndi ziti zomwe zinayenda bwino?
- Ndi ziti zomwe sizinayende bwino?.
- Kodi mukuyenera kusintha zinthu ziti pa ndondomeko yanu?.
- Kodi zosatira zinali monga munafunila? Ngati sichoncho chifukwa chiyani?
- Kodi Mulungu analemekezeka

Ophunzitsa ali ndi fomu ya lipoti yoti akupaseni. Kodi ndi chifukwa ninji timayenera kupeleka lipoti? Marko 6:30 , tikuona kuti ophunzira anapeleka lipoti kwa yesu zinthu zonse zimene anachita. Timapeleka lipoti pofuna kuonetsa kukhulupilika ndi kuyamika kwa iwo amene atiphunzitsa ndikutikonzera zofunika ndi kutipatsa aphunzitsi. Lipoti imatithandiza kukhala ndid mwayi ogawana ndi anzthu chimene tinachita ndipo chimapeleka umboni za mmene mulungu anakugwilitsilani ntchito. Lipoti imapelekanso mwayi kwa ophunzitsa kuona ngati panali mabvuto ndikuona ngati panali mabvuto ndikupeza njira yabwino yokuthandizirani mtsogolo

Ma fomu adogosolo

	Chani	Oyendetsa	Nthawi
Zipangizo			
Anthu okhudzidwa			
Anthu opindula			
Chilolezo			
Pemphero			

Tsiku	Ma sitepe	Zofunika	Oyendetsa